



Mfundo zachitukuko chokhazikika



CHICHEWA

MFUNDO ZACHITUKUKO CHOKHAZIKIKA

Izi ndi nsanamira za zofuna za anthu, mfundo zothetsera umphawi mmagawo onse mosabwelera mmbuyo ndi pochitira zinthu limodzi - **Ban Ki-moon**



CHOLINGA 1



Kuthetseratu umphawi wamtundu wina uliwonse, kulikonse

- 1.1 Kuthetsa umphawi wadzawoneni pakati pa anthu onse pofika mchaka cha 2030, kwa anthu amene amalephera kupeza ndalama yokwanira 1.25 US Dollar pa tsiku.
- 1.2 Kuchepetsa ndi theka umphawi pakati pa abambo, amayi ndi ana onse pofika mchaka cha 2030 molingana ndi mmene dziko limatathauzira umphawi.
- 1.3 Kukhazikitsa njira zoyenera zothandizira anthu osauka ndi amene ali pachioopsyezo mdziko pofika mchaka cha 2030.
- 1.4 Kuwonetsetsa kuti abambo ndi amayi makamaka osauka ndi amene ali ndi mwayi ofanana pakapezedwe ka chuma ndi zinthu zina zofunika pa moyo wao monga; malo, katundu, luso la makono loyenera ndi chuma monga mwayi wa ngongole zing'onozing'ono pofika mchaka cha 2030.
- 1.5 Kulimbikitsa anthu osauka ndi omwe ali pachioopsyezo kukhala ndikuthekera komanso kupilira, kuthana ndi mavuto ogwa mwadzidzidzi monga a zanyengo, zachuma ndi zachilengedwe pofika mchaka cha 2030.
- 1.a Kuwonetsetsa kuti zipangizo zofunikira zikusokhanitsidwa kuchokera mbali zosiyansiyana monga kudzera mu mgwirizano wa zachitukuko ndi cholinga chopereka njira ku maiko okwera kumene makamaka osauka kuti athe kukhazikitsa ndondomeko ndi ntchito zoyenera zothetsera umphawi.
- 1.b Kukonza ndondomeko zabwino mdziko, mzigawo ndi dziko lonse lapansi zokomera anthu osauka komanso posayang'anira kusiyana pakati pa amayi ndi abambo polimbikitsa kuthandizira kukhazikitsa ntchito zabizinesi zothetsera umphawi.

CHOLINGA 2

Kuthetsa njala, kukhala ndi chakudya chokwanira chamagulu ndi kulimbikitsa ulimi wamakono



- 2.1 Kuthetsa njala pakati pa anthu osauka ndi amene ali pachipyezo kuphatikizapo ana osaposeza zaka ziwiri zakubadwa, kukhala ndichakudya chokwanira, chotetezeka ndi chamagulu chaka chonse pofika mchaka cha 2030.
- 2.2 Kuthetsa kunyentchera pofika mchaka cha 2030 pokwaniritsa mulingo wadziko lonse lapansi wothetseratu kupinimbira kwa ana osaposeza zaka zisanu zakubadwa pofika mchaka cha 2025, kulimbikitsa atsikana otha msinkhu, amayi oyembekezera ndi oyamwitsa komanso okalamba kudya zakudya za magulu.
- 2.3 Kuchulukitsa zokolola ndi ndalama zomwe alimi ang'onoang'ono amapeza, makamaka amayi, anthu akumudzi, alimi a ziweto ndi asodzi kudzera pokhala ndi malo olima okwanira, kupeza zipangizo zaulimi, ukadaulo wamalimidwe wamakono, njira zopezera ndalama, misika ndi njira zina zochulukitsira zokolola pofika mchaka cha 2030.
- 2.4 Kulimbikitsa njira zopezera chakudya chokwanira ndikukhazikitsa njira zokhazikika zaulimi zosawononga chilengedwe, polimbikitsa kulimbana ndi kusintha kwa nyengo, ng'amba, kusefukira kwa madzi ndi mavuto ena ogwa mwadzidzidzi ndi cholinga chofuna kuteteza chonde mu nthaka pofika mchaka cha 2030.
- 2.5 Kugwiritsa ntchito mbeu zamakono mwakasinthasinth, kusunga ziweto ndikusamalira nyama za mtchire kudzera posunga mbeu ndi nyama mmalo oyenera okhazikitsidwa mdziko, mzigawo ndi dziko lonse. Kulimbikitsa kupeza ndi kugawana phindu lopezeka pogwiritsa ntchito nzeru zopezeka mdziko zovomerezeka ndi maiko onse adziko lonse pofika mchaka cha 2020.
 - 2.a Kulimbikitsa kafukufuku wa zaulimi ndikupereka ulangizi ndi luso kwa alimi komanso kukhala ndi nkhothe yosungira mbeu zaziweto ndi zomera polimbikitsa kupeza phindu lochuluka pa ulimi mmaiko okwera kumene ndi osauka kudzera mu mgwirizano wa maiko onse.
 - 2.b Kuunikanso malamulo ndi zolepheretsa pa nkhani zamalonda azaulimi padziko lonse lapansi kuphatikizapo kuthetsa mchitidwe omwe maiko ena amachita owonjezera ndalama pamwamba ndi cholinga chakuti ogulitsa apezephindu lochuluka pogulitsa malonda azaulimi kunja kwa dziko, molingana ndi mgwirizano wazachitukuko wa Doha (Doha Development Round).
 - 2.c Kutsata ndondomeko zowonetsetsa kuti misika ya zaulimi ikuyenda bwino ndikuwonetsetsa kuti alimi akupeza mauthenga azamisika ndi malo osungira zokolola mu nthawi yake pothandiza kuteteza kusinthasinth kwa mitengo yazakudya.



CHOLINGA 3



Kupititsa patsogolo umoyo wabwino wa anthu onse

- 3.1 Kuchepetsa imfa za amayi woyembekezera kufika pamulingo wa 70 pa amayi 100,000 pofika mchaka cha 2030
- 3.2 Kuchepetsa imfa zopeweka kwa ana obadwa kumene ndi omwe zaka zawo sizinafike zisanu, ndicholinga chakuti maiko onse achepetse imfa za ana obadwa kumene kuti zichepere mulingo ochepera ana 12 mwa 1,000 ali wonse ndi mulingo wa 25 pa ana 1,000 osapitilira zaka zisanu pofika mchaka cha 2030.
- 3.3 Kuthetsa Edzi, matenda a chifuwa chachikulu, malungo ndi matenda ena monga likodzo, kamwazi ndi kutsegula mmimba, matenda okhudza chiwindi ndi ena opatsirana pofika mchaka cha 2030.
- 3.4 Kuchepetsa imfa za ana, mmodzi mwa ana atatu obadwa masiku osakwanira ku matenda opatsirana powateteza, kuchiza ndi kulimbikitsa umoyo wabwino ndi kuthana ndi nthenda za mu ubongo pofika mchaka cha 2030.
- 3.5 Kulimbikitsa kupewa ndi kuchiza matenda omwe amabwera chifukwa chogwiritsa ntchito mankhwala ozunguza ubongo ndikumwa mowa mwa uchidakwa.
- 3.6 Kuchepetsa ndi theka kuvulala ndi imfa zomwe zimachitika chifukwa cha ngozi za pamseu pofika mchaka cha 2020
- 3.7 Kuwonetsetsa kuti anthu akupeza thandizo, mauthenga ndi maphunziro azakugonana ndi uchembere wabwino monga kulera ndi kukhazikitsa ntchitozi mu dongosolo laboma la zaumoyo pofika mchaka cha 2030
- 3.8 Kukwaniritsa kufikira anthu onse ndi ntchito zaumoyo, kuwateteza ku zotsamwitsa za chuma, kupezetsa chisamaliro cha zaumoyo choyenera, kupeza mankhwala otsika mtengo ndi katemera kwa aliyese
- 3.9 Kuchepetsa imfa ndi matenda zomwe zimabwera chifukwa cha mankhwala owopsa ndi kuwonongeka kwa mpweya, madzi ndi nthaka pofika mchaka cha 2030
- 3.a Kulimbikitsa ndi kutsatira lamulo loletsa kusuta fodya mmaiko onse motsatira mgwirizano wa bungwe lalikulu la zaumoyo pa dziko lonse (WHO)
- 3.b Kuthandiza ntchito zakafukufuku wakatemera ndi mankhwala amatenda onse opatsirana ndi opatsirana omwe akuvutitsa mmaiko okwera kumene, ndikuwapatsa mankhwala otsika mtengo ndi katemera molingana ndi zomwe anagwirizana ku msonkhano wa zaumoyo waku Doha (Doha Declaration on the TRIPS Agreement and Public Health)
- 3.c Kulimbikitsa kuwonjezera ndalama zoyendetsera ntchito zaumoyo, kuphunzitsa, kulemba ntchito anthu azaumoyo ndikuwonetsetsa kuti sakusiya ntchito mmaiko okwera kumene
- 3.d Kuwapatsa kuthekera, luntha ndi luso maiko onse makamaka osaukitsitsa kuti athe kukonzekera, kuchepetsa ndi kuthana ndi ziwopsezo zokhudza umoyo



CHOLINGA 4



Kulimbikitsa ndi kupititsa patsogolo mwayi wamaphunziro abwino kwa wina aliyense

- 4.1 Kuwonetsetsa kuti achinyamata akumaliza maphunziro aulere ndi apamwamba a kupulayimale ndi sekondale mofanana pofika mchaka cha 2030.
- 4.2 Kuwonetsetsa kuti ana ang'ono akupeza maphunziro a mmera mpoyamba powakonzekeretsa maphunziro a kupulayimale pofika mchaka cha 2030
- 4.3 Kuwonetsetsa kuti amayi ndi abambo akupeza mwayi wofanana komanso osavuta pamaphunziro apamwamba aluso la ntchito zamanja ndi sukulu za ukachenjede pofika mchaka cha 2030
- 4.4 Kuchulutsa chiwerengero cha achinyamata ndi achikulire omwe ali ndi luso lantchito zamanja kuti apeze ntchito zabwino kapena kuyamba bizinesi pofika mchaka cha 2030
- 4.5 Kuthetsa kusankhana pakati pa amayi ndi abambo pamaphunziro ndikuwonetsetsa kuti akulandira mwayi ofanana pamaphunziro ndi luso lantchito zamanja powaganiziraso anthu ovutika monga a ulumali, anthu akumudzi ndi ana osowa pofika mchaka cha 2030
- 4.6 Kuwonetsetsa kuti achinyamata ndi achikulire akutha kulemba ndi kuwerengera pofika mchaka cha 2030
- 4.7 Kuwonetsetsa kuti ophunzira akulandira luntha ndi luso lofunikira kupititsa patsogolo chitukuko kudzera mmaphunziro, umoyo wa bwino, ufulu wa chibadwidwe, kupereka mwayi ofanana pakati pa amayi ndi abambo, ndi kupititsa patsogolo mtendere, kulolerana kusiyana kwa zikhalidwe mwa zina, polimbikitsa chitukuko pofika mchaka cha 2030
- 4.a Kumanga ndi kukonzanso malo ophunzilira kuti akhale okomera ana onse kuphatikizapo a ulumali osiyanasiya komanso kuwonetsetsa kuti malowa ali ndi chitetezo chokwanira
- 4.b Kuchulukitsa chiwerengero cha anthu othandizidwa ndi ndalama za maphunziro ku maiko amene akukwera kumene makamaka osaukitsitsa ndi cholinga chakuti apeze maphunziro aukachenjede, za luso la ntchito za manja, zofalitsira unthenga kudzera mmakina a intaneti ndi sayansi kuchokera ku maiko olemera pofika mchaka cha 2020
- 4.c Kuchulukitsa chiwerengero cha aphunzitsi ophunzitsidwa bwino kudzera mu mgwirizano wa aphunzitsi a maiko okwera kumene makamaka osaukitsitsa pofika mchaka cha 2030



CHOLINGA 5



Kukwaniritsa ndondomeko za kusasankhana pakati pa amayi ndi abambo ndikuwapatsa amayi ndi atsikana mwayi wodziyimira pawokha

- 5.1 Kuthetsa mchitidwe osala amayi ndi atsikana pena paliponse
- 5.2 Kuthetsa mchitidwe wankhanza kwa amayi ndi atsikana mmalo osiyanasiyana kuphatikizapo mchitidwe ozembetsa amayi ndi atsikana, kuwagwililira ndi kuwapangira nkhanza zina zosiyanasiyana
- 5.3 Kuthetsa mchitidwe oyipa monga kukwatitsa ana mowakakamiza ali achichepere ndi kuthetsa mdulidwe wa atsikana
- 5.4 Kukhazikitsa ndi kulimbikitsa ndondomeko zotetezera ogwira ntchito ya mnyumba omwe salandira malipiro powonetsetsa kuti magwiridwe a ntchito akugawidwa mofanana kwa wina aliyese
- 5.5 Kuwonetsetsa kuti amayi akupatsidwa mwayi wa utsogoleri mmagawo onse komanso kupatsidwa mwayi wopereka maganizo awo pandale, chuma ndi kayendetsedwe ka dziko
- 5.6 Kuwonetsetsa kuti anthu onse ali ndi ufulu opeza thandizo la uchembere wabwino motsatira ndondomeko za mgwirizano wamsonkhano wachitukuko ndi chiwerengero cha anthu womwe unachitikira ku Beijing mdziko la China
- 5.a Kusintha kagwiridwe ka ntchito pofuna kupereka ufulu ofanana kwa amayi opeza chuma, kukhala ndi ulamuliro wa malo, ndi kupeza mwayi wokhala ndi katundu, ngongole ndi zachilengedwe mogwirizana ndi malamulo adziko
- 5.b Kulimbikitsa kugwiritsa ntchito zipangizo zaluso lamakono lofalitsira unthenga kwa amayi kuti athe kudziyimira pawokha
- 5.c Kutsatira ndi kulimbikitsa ndondomeko zaboma ndi malamulo pofuna kupititsa patsogolo kusasankhana pakati pa amayi ndi abambo ndi kupereka mphamvu kwa amayi ndi atsikana kuti athe kudziyimira pawokha



CHOLINGA 6



Kulimbikitsa kupezeka ndi kusamala madzi ndi ukhondo kwa anthu onse

- 6.1 Kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza madzi akumwa abwino mosavuta pofika mchaka cha 2030
- 6.2 Kukwaniritsa ukhondo ndi kutsatira ndondomeko zosamalira pankhomo ndi pathupi, kusiya kunyera kutchire moganizira zofunika za amayi ndi atsikana ndi ena onse ovutika pofika chaka cha 2030
- 6.3 Kupititsa patsogolo kupezeka kwa madzi abwino pochepetsa kuwonongeka kwa madzi pothetsa mchitidwe wotayira mankhwala ndi nyansi paliponse, kuchepetsa ndi theka madzi oyipitsidwa ndi mankhwala, ndi kuwakonzanso kuti athe kugwiritsidwa ntchito zina zomwe sizingapereke chiwopsyezo pa umoyo wamunthu pofika mchaka cha 2030
- 6.4 Kuwonetsetsa kuti mabungwe ndi anthu ena onse akugwiritsa ntchito madzi mosamala ndicholinga chakuti madzi abwino asamasowe, ndikuchepetsa chiwerengero cha anthu chosowa madzi abwino pofika mchaka cha 2030
- 6.5 Kugwira ntchito zosamalira madzi mogwirizana mmagawo onse posayangánira malire amaiko pofika mchaka cha 2030
- 6.6 Kuteteza ndi kubwezeretsa zachilengedwe zomwe zimasunga madzi monga mapiri, nkhalango, madambo, mitsinje, akasupe ndi nyanja pofika mchaka cha 2020
- 6.a Kulimbikitsa mgwirizano wamaiko onse waluso ndi luntha lamaiko omwe akukwera kumene pakagwiridwe kantchito zamadzi ndi ukhondo monga kukolora madzi, kuthira mankhwala mmadzi akumwa, kuthira mankhwala mmadzi oyipa, kukonzanso madzi oyipa pogwiritsa ntchito njira zamakono pofika mchaka cha 2030
- 6.b Kuthandiza ndi kulimbikitsa anthu akumudzi kutenga gawo posamalira madzi ndi kuyendetsa ntchito zaukhondo

CHOLINGA 7



Kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza mphamvu yamagetsi yodalirika, yokhazikika, yamakono ndi yotsika mtengo

- 7.1 Kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza magetsi odalirika, okhazikika, amakono ndi otsika mtengo pofika mchaka cha 2030
- 7.2 Kuchulukitsa kagawidwe kamagetsi ochokera ku mphamvu zosiyanasiyana monga yadzuwa kapena mphepo pofika mchaka cha 2030
- 7.3 Kuchulukitsa mulingo ogwiritsa ntchito magetsi mosamala pa dziko lonse pofika mchaka cha 2030
 - 7.a Kulimbikitsa mgwirizano wamaiko popititsa patsogolo kafukufuku ndi luso lamakono lantchito yopanga magetsi kuchokera kumphamvu yadzuwa, kugwiritsa ntchito mphamvu zochokera ku chilengedwe monga malasha ndi petulo komanso kulimbikitsa zomangamanga za ntchito yamagetsi pofika mchaka cha 2030
 - 7.b Kukuza ntchito zomangamanga ndi kukweza luso loperekera ntchito zamakono, zokhazikika zamagetsi ku maiko okwera kumene makamaka osauka potsatira ndondomeko zothandizira ntchito zamagetsi pofika mchaka cha 2030

CHOLINGA 8



Kupititsa patsogolo chuma ndi kupezetsa ntchito zabwino zokhazikika kwa anthu onse

- 8.1 Kulimbikitsa kukweza chuma chomwe munthu akupeza molingana ndi mmene chuma chadziko chikuyendera makamaka powonetsetsa kuti chumacho chikukwera ndi magawo 7 pa 100 (7%) aliwonse pachaka mmaiko osauka
- 8.2 Kukwaniritsa kukwera kwa chuma pogwiritsa ntchito njira zatsopano zosiyanasiyana pakupititsa patsogolo luso ndi kubweretsa njira zamakono zochitira zinthu, ndi maganizo opanga katundu wapamwamba polemba anthu ochuluka ogwira ntchito
- 8.3 Kulimbikitsa ndondomeko zachitukuko, zabizinesi, maganizo atsopano akachitidwe kazinthu, kupezetsa anthu ntchito, kukhazikitsa ndi kukweza mabizinesi ang'onoang'ono ndi kuwapezetsa ngongole
- 8.4 Kulimbikitsa kupanga ndi kagwiritsidwe ntchito kazinthu moyenera, pokweza chuma ndi kusamala za chilengedwe potsata ndondomeko ya dziko lonse yolimbikitsa kupanga ndi kugwiritsa ntchito zinthu moyenera (10-Year Framework of Programmes on Sustainable Consumption and Production) motsogozedwa ndi maiko otukuka pofika mchaka cha 2030
- 8.5 Kupezetsa amayi, abambo, achinyamata ndi anthu aulumali ntchito zokhazikika, ndikuwonetsetsa kuti akulandira malipiro ofanana molingana ndi ntchito zimene akugwira pofika mchaka cha 2030
- 8.6 Kuchepetsa chiwerengero cha achinyamata chomwe sichili pantchito ndi chosapita kusukulu pofika mchaka cha 2020
- 8.7 Kuthetsa mchitidwe wokakamiza munthu kugwira ntchito, kuthetsa thangata, kuzembetsa anthu ndi kupeza njira zothetseratu kulemba ana ntchito zoposa msikhu wawo ndi kuwalemba usilikali pofika mchaka cha 2025
- 8.8 Kuteteza ufulu wa ogwira ntchito ndikuwonetsetsa kuti malo antchito ali ndi chitetezo chokwanira kwa onse kuphatikiza anthu ochokera mmaiko ena makamaka amayi
- 8.9 Kukhazikitsa ndondomeko zotukula ntchito zokopa alendo zomwe zingapereke mwayi wantchito kwa anthu ndikulimbikitsa chikhalidwe ndi katundu opangidwa ndi ntchito yopanga katundu mdziko pofika mchaka cha 2030
- 8.10 Kulimbikitsa ntchito zamabungwe azachuma kuti anthu athe kufikira ku mabanki, inshulasi ndi mabungwe obwereketsa ndi kusungitsa ndalama
- 8.a Kupereka thandizo lopititsa patsogolo ntchito zamalonda kumaiko osauka
- 8.b Kukhazikitsa ndondomeko yolembe ntchito achinyamata potsatira mgwirizano omwe unakhazikitsidwa ndi bungwe lowona za anthu a pantchito padziko lonse (Global Jobs Pact of the International Labour Organization) pofika mchaka cha 2020



8 DECENT WORK AND
ECONOMIC GROWTH



PERSONS AFFAIRS
EDUCATION AND TRAINING
SECONDARY
MUNICIPALITY

CHOLINGA 9

Kumanga zinthu zolimba, kulimbikitsa ntchito za mafakitale ndi luntha latsopano lakachitidwe ka zinthu



- 9.1 Kumanga zinthu zapamwamba, zolimba ndi zodalirika zolumikizitsa madera ndi maiko pokweza ntchito zachitukuko ndi umoyo wa anthu
- 9.2 Kulimbikitsa ntchito zamafakitale ndicholinga chokweza chiwerengero cha anthu olembedwa ntchito ndi kuchulukitsa katundu wopangidwa mmafakitale potukula chuma chadziko komanso kuchulukitsa mulingo wachuma chomwe maiko osauka amapeza pofika mchaka cha 2030
- 9.3 Kuchulukitsa mwayi wa mafakitale ndi mabizinesi ang'onoang'ono kupeza ngongole zokhala ndi chiwongola dzanja chotsika ndi kuwapezera misika makamaka maiko okwera kumene
- 9.4 Kukweza ntchito zomangamanga ndi mafakitale kuti zikhale zokhazikika komanso kugwiritsa ntchito zipangizo moyenera pogwiritsa ntchito luso loteteza zachilengedwe molingana ndi kuthekera kwa maiko pofika mchaka cha 2030
- 9.5 Kulimbikitsa kafukufuku wa sayansi, luso lamakono la mafakitale mmaiko onse, makamaka okwera kumene, kulimbikitsa kuchita zinthu mwatsopano powonjezera chiwerengero cha anthu ogwira ntchito zakafukufuku ndi chitukuko pa anthu 1 miliyoni aliwonse ndi kuonjezera ndalama zogwirira ntchito za kafukufuku m'boma ndi mmakampani pofika chaka cha 2030
- 9.a Kuthandizira kupititsa patsogolo chitukuko cha zomangamanga mmaiko okwera kumene popeleka thandizo landalama, luso ndi ukadaulo ku maiko a mu Africa ndi ena osauka.
- 9.b Kutukula ntchito zaluso lamakono lachitukuko, kafukufuku ndi kuchita zinthu mwatsopano mmaiko okwera kumene kuti pakhale ndondomeko zabwino zamafakitale kuti azikwanitsa kupanga katundu osiyanasiyana wapamwamba
- 9.c Kuwonetsetsa kuti anthu akupeza mauthenga ndi luso la lamy kudzera mmakina a kompyuta mosavuta pa mtengo wotsika, mmaiko osauka pofika chaka cha 2020

CHOLINGA 10

Kuchepetsa kusiyana pakachitidwe kazinthu mdziko ndi pakati pamaiko ena



- 10.1 Kukwaniritsa kukweza chuma kwa anthu 40 pa 100 (40%) osauka aliwonse kupita pa mulingo okwera kutengera mulingo omwe boma limagawira chuma chake pa munthu mmodzi pofika mchaka cha 2030
- 10.2 Kupereka mphamvu kwa anthu, kulimbikitsa chikhalidwe, chuma ndi ndale kwa anthu onse posayangánira zaka, chibadwidwe, ulumali, mtundu, kochokera, chipembedzo ndi mapezedwe achuma.
- 10.3 Kuwonetsetsa kuti anthu akukhala ndi mwayi wofanana pothetsa kusiyana pakachitidwe kazinthu, kuthetsa malamulo ndi ndondomeko zolimbikitsa kusalana
- 10.4 Kutsatira ndondomeko zakagwiritsidwe ntchito kandalama zaboma, malipiro, zothandizira anthu ovutika powonetsetsa kuti anthu akupeza zinthu mofanana
- 10.5 Kupititsa patsogolo ndi kulimbikitsa malamulo ndi kupanga kauniuni wamisika ndi mabungwe azachuma padziko lonse
- 10.6 Kuwonetsetsa kuti maiko osauka ali ndi owayimilira komanso kutha kupereka maganizo awo mmisokhano ya mabungwe azachuma adziko lapansi polimbikitsa kuchita zinthu poyera
- 10.7 Kuthandizira anthu kuyenda ndikutha kulowa mmaiko ena popanda vuto pogwiritsa ntchito ndondomeko zomwe zimatsatidwa powona anthu olova ndi kutuluka maiko awo moyenera
- 10.a Kukhazikitsa mfundo zapadera ndi kuchepetsa mchitidwe osiyanita popereka thandizo lazamalonda kumaiko okwera kumene makamaka osauka potsatira mgwirizano wabungwe lamalonda padziko lonse. (World Trade Organization agreements)
- 10.b Kulimbikitsa ntchito zachitukuko ndi zachuma monga maiko otukuka kuyambitsa mabizinesi kumaiko osauka monga amu Africa molingana ndi ndondomeko zomwe maiko anakhazikitsa
- 10.c Kuchepetsa mulingo wandalama zomwe anthu amalipira akamachoka mdziko lawo kupita kudziko lina kuchepera pa 3 pa 100 (3%) ina iliyonse ndi kuchotsa ndalama zomwe anthu amapereka akamadutsa mdziko la eni kupita mdziko lina ngati zikudutsa mulingo wa 5 pa 100 (5%) ina iliyonse pofika mchaka cha 2030

CHOLINGA 11



Mizinda ndi malo ena okhala anthu akhale okomera wina aliyense, otetezeka ndi okhazikika

- 11.1 Kuwonetsetsa kuti nyumba zikupezeka zokwanira ndi zodalirika pa mtengo otsika pofika mchaka cha 2030
- 11.2 Kupereka mayendedwe abwino, otsika mtengo ndi odalirika, kupititsa patsogolo chitetezo cha pamseu pokuza ntchito zamayendedwe moganizira anthu amene ali ovutika monga amayi, ana, anthu aulumali ndi okalamba pofika mchaka cha 2030
- 11.3 Kukhazikitsa ndondomeko zodalirika ndi kayendetsedwe kamizinda kokomera anthu mmaiko onse pofika mchaka cha 2030
- 11.4 Kulimbikitsa ntchito zoteteza malo onse omwe ali ndi mbiri ndi chikhalidwe
- 11.5 Kuchepetsa chiwerengero cha imfa ndi anthu okhudzidwa ndi ngozi zosiyanasiyana monga kusefukira kwa madzi poteteza anthu ovutika ndi cholinga chochepetsa ndalama zogwilira ntchito yoteteza anthu padziko lonse pofika mchaka cha 2030
- 11.6 Kuchepetsa mavuto omwe munthu okhala mu mzinda amakumana nawo chifukwa cha kuwonongeka kwachilengedwe powonetsetsa kuti anthu akupuma mpweya wabwino ndipo kuwonetsetsa kuti zinyalala zikutayidwa malo oyenera pofika mchaka cha 2030
- 11.7 Kupereka malo abwino, odalirika, okomera anthu onse makamaka amayi, ana, achikulire ndi anthu aulumali
- 11.a Kulimbikitsa mgwirizano pankhani zachuma, chikhalidwe ndi zachilengedwe pakati pamizinda ndi madera akumidzi popanga ndondomeko zachitukuko zabwino
- 11.b Kuchulutsa mizinda ndi malo ena okhala anthu potsatira ndondomeko zogwiritsa ntchito zinthu moyenera, kutsatira njira zabwino zotetezera zachilengedwe ndi ngozi potsatira mgwirizano womwe maiko anapanga ku Sendai (Sendai Framework for Disaster Risk Reduction 2015-2030) pofika mchaka cha 2020
- 11.c Kuthandiza maiko osauka pankhani zachuma ndi luso pomanga zinthu zodalirika monga nyumba pogwiritsa ntchito zipangizo zakuderako



CHOLINGA 12

Kulimbikitsa ndi kugwiritsa ntchito katundu moyenera



- 12.1 Maiko onse atsatiye ndondomeko ya zaka 10 (*10-Year Framework of Programmes on Sustainable Consumption and Production Patterns*) yopanga ndi kugwiritsa ntchito katundu moyenera, motsogozedwa ndi maiko olemera poganizira chitukuko ndi kuthekera kwamaiko okwera kumene
- 12.2 Kukwaniritsa kuyangánira ndi kugwiritsa ntchito zinthu zachilengedwe moyenera pofika mchaka cha 2030
- 12.3 Kuchepetsa ndi theka kuwonongeka kwa chakudya chamunthu padziko kuyambira kogulitsa ndi kogula komanso ku mafakitale, popititsa kumisika ndi zokolola pofika mchaka cha 2030
- 12.4 Kukwaniritsa kusamalira mankhwala owopsya ndi zinyasi molingana ndi mgwirizano wamaiko onse pochepetsa kuwononga mpweya, madzi ndi nthaka poteteza umoyo wa anthu ndi chilengedwe pofika mchaka cha 2020
- 12.5 Kuchepetsa zinyansi pozikonzanso ndikuzigwiritsa ntchito mu mnjira zina pofika mchaka cha 2030
- 12.6 Kulimbikitsa makampani makamaka akuluakulu omwe akupezeka mmaiko osiyanasiyana kutsata ndi kukhazikitsa njira zodalirika zogawanirana uthenga pantchito zawo
- 12.7 Kulimbikitsa njira zodalirika zogulira katundu ofunika kwambiri motsatira ndondomeko za dziko
- 12.8 Kuwonetsetsa kuti anthu akulandira uthenga owadziwitsa ndi kuzindikiritsa zinthu zachitukuko ndi umoyo wawo mogwirizana ndi zachilengedwe pofika mchaka cha 2030
- 12.a Kuthandiza maiko okwera kumene pantchito zaluso ndi sayansi zokhazikika kuti azitha kupanga katundu ndikumugwiritsa ntchito moyenera
- 12.b Kupanga ndi kutsata njira zopangira kauniuni wantchito zachitukuko polimbikitsa zokopa alendo zomwe zimapezetsa mwayi wantchito ndi cholinga chopititsa patsogolo chikhalidwe ndi zinthu zopangidwa kudera
- 12.c Kuunikanso ndalama yomwe imawonjezedwa pa mafuta pofuna kuchepetsa kugwiritsa ntchito zinthu mowononga komanso kuchotsa zinthu zomwe zimasokoneza malonda pamsika molingana ndi momwe zinthu zikuyendera mdziko ndi pakukonzanso ntchito zamisonkho, kuchotsa ndalama yomwe imawonjezedwa pamtengo wakatundu wogulitsira kuti atsike mtengo poganizira zofuna zamaiko okwera kumene ndi ndondomeko zoteteza anthu osauka ndi madera okhudzidwa



CHOLINGA 13

Kupanga changu pokhazikitsa mfundo zolimbana ndi kusintha kwa nyengo



- 13.1 Kulimbikitsa luso ndi kuthekera kwa maiko onse polimbana ndi kusintha kwa nyengo ndi mavuto ogwa mwadzidzidzi
- 13.2 Kulumikizitsa mfundo zolimbana ndi kusintha kwa nyengo mu ndondomeko zoyendetsera boma
- 13.3 Kulimbikitsa kuphunzitsa ndi kudziwitsa anthu ndi mabungwe kuti akhale ndi kuthekera kolimbana ndi ziopsyezo zomwe zimabwera chifukwa cha kusintha kwa nyengo
- 13.a Kukhazikitsa chimvano chomwe maiko olemera anamvana ku msonkhano wamaiko onse okambirana zakusintha kwa nyengo ndi cholinga choti azisokhanitsa pamodzi ndalama yokwana \$100 billion chaka chilichonse kuchokera kumbali zosiyanasiyana pofika mchaka cha 2020 ndi cholinga chokwaniritsa zofuna za maiko okwera kumene kuti ntchito yolimbana ndi kusintha kwa nyengo izichitika mosabisa kanthu
- 13.b Kulimbikitsa njira zopititsira patsogolo luso ndi kuthekera kwa maiko osauka kuti athe kulimbana ndikusintha kwa nyengo molingana ndi ndondomeko za maiko okwera kumene poganizira amayi, achinyamata ndi magulu osalidwa



CHOLINGA 14

Kusamala ndi kugwiritsa ntchito moyenera nyanja ndi zinthu zopezeka mnyanjamo polimbikitsa ntchito za chitukuko chokhazikika



- 14.1 Kuwonetsetsa kuti ntchito zomwe zikugwiridwa ku mtunda sizikuwononga zinthu za moyo zopezeka mmadzi pofika mchaka cha 2025
- 14.2 Kusamalira ndi kuteteza zamoyo za mnyanja ndi mmbali mwa nyanja polimbikitsa ntchito yobwezeretsa zowonongeka kuti nyanja zizikhala za phindu ndi ukhondo pofika mchaka cha 2020
- 14.3 Kuchepetsa ndi kukonza kuwonongeka kwa nyanja komwe kumakhudza zamoyo podzera mu mgwirizano wa maiko pa ntchito zaluso ndi sayansi mmagawo onse
- 14.4 Kukhazikitsa malamulo othetsa kukolola ndi kumpha nsomba mwachisawawa ndi kukhazikitsa njira za makono zobwezeretsa nsomba mukanthawi kochepa ndi cholinga chakuti zithe kuswana mochuluka pofika mchaka cha 2020
- 14.5 Kusamalira magawo 10 pa 100 aliwonse a zamoyo zopezeka mmadzi ndi mmbali mwa nyanja mogwirizana ndi malamulo adziko komanso dziko lonse pogwiritsa ntchito uthenga ovomerezeka wa sayansi pofika mchaka cha 2020
- 14.6 Kuletsa njira zina zomwe asodzi amathandiziridwa zimene zikupangitsa kuwedza nsomba mowononga ndikuletsa kukhazikitsa njira zina zothandizira asodzi zomwe zingapangitse kuti asamatsatire njira zovomerezeka za usodzi, mowaganizira maiko okwera kumene ndi osauka kuti azitenga nawo gawo pa zokambirana zothandizira asodzi ku bungwe lazamalonda pa dziko lonse (World Trade Organization) pofika mchaka cha 2020
- 14.7 Kuonjezera thandizo lachuma ku maiko osauka polimbikitsa kagwiritsidwe ntchito ka zinthu zopezeka mmadzi polimbikitsa njira zabwino zausodzi ndi zokopa alendo pofika mchaka cha 2030
- 14.a Kuonjezera nzeru ndi luso la sayansi, kukweza kuthekera kwa kafukufuku ndi kugawana luntha lokhudza zamoyo za mmadzi poganizira ndondomeko za maiko amene malire awo ali nyanja yamchere (Intergovernmental Oceanographic Commission Criteria) ndi ndondomeko zogawana luso la za moyo za mmadzi (Guidelines on the Transfer of Marine Technology), ndi cholinga chopititsa patsogolo umoyo wa zamnyanja ndi kulimbikitsa kusamalira zamoyo zopezeka mnyanja moganizira chitukuko cha maiko osauka
- 14.b Kupereka mwayi kwa asodzi angónoangóno opeza zinthu mmadzi ndi kuwapezetsa misika
- 14.c Kulimbikitsa kusamalira nyanja ndi zopezeka mnyanjamo pokhazikitsa malamulo okhudza maiko onse monga analembdewera ndi bungwe la dziko lonse okhudzana ndi zanyanja (United Nations Convention on the Law of the Sea), omwe gawo 158 likutsindika kuti “Tsogolo lomwe tikufuna”



14 LIFE BELOW WATER



CHOLINGA 15



Kuteteza, kubwezeretsa, ndi kulimbikitsa kagwiritsidwe ntchito ka za moyo za pa mtunda ndi kusamala nkhalango, kuthetsa chipululu ndi kuwonongeka kwa nthaka

- 15.1 Kusamalira, kubwezeretsa ndi kulimbikitsa kagwiritsidwe ntchito kazamoyo zopezeka pa mtunda ndi zamoyo zopezeka mnyanja ndi ntchito zake makamaka nkhalango, madambo, mapili ndi kumtunda motsatira migwirizano ya dziko lonse pofika mchaka cha 2020
- 15.2 Kulimbikitsa kusamalira nkhalango zonse, kuthetsa kudula mitengo, kubwezeretsa nkhalango zowonongeka ndi kulimbikitsa kudzalanso mitengo padziko lonse pofika mchaka cha 2020
- 15.3 Kuthana ndi vuto la chipululu, kubwezeretsa nthaka yoguga kuphatikizapo malo amene apanga chipululu okhudzidwa ndi kusowa kwa mvula ndi madzi osefukira polimbikitsa kuthetsa kuwonongeka kwa nthaka padziko lonse pofika mchaka cha 2030
- 15.4 Kulimbikitsa kusamalira zachilengedwe zopezeka mmapi, polimbikitsa kuthekera kuti zithe kupindulira mmadera opezeka pachitukuko chokhazikika pofika mchaka cha 2030
- 15.5 Pofunika kuchita kanthu mwa msanga pochepetsa kuwonongeka kwa malo achilengedwe, kuthetsa kuwonongeka kwa zamoyo zopezekamo ndikuteteza zolengedwa zomwe zili pachiwopsyezo chakuti zikhonza kutha pofika mchaka cha 2020
- 15.6 Kugawana mofanana phindu lochokera ku kagwiritsidwe ntchito ka zinthu zomwe zili ndi phindu ndi kulimbikitsa kuti zinthuzo zizipezeka mosavuta malinga ndi mgwirizano wamaiko osiyanasiyana
- 15.7 Kuchita zinthu mwa msanga pofuna kuthetsa kupha nyama mopanda chilolezo ndi kuthana ndi kuzembetsa nyama ndi zomera zotetezedwa komanso kuthana ndi kugula ndi kugulitsa mosavomerezeka
- 15.8 Kukhazikitsa njira zopewera kubweretsa zamoyo ku malo komwe sizikuyenera kukhala monga mmadzi kapena ku mtunda
- 15.9 Kuwonetsetsa kuti ndondomeko zachitukuko cha dziko kapena cha kudera komanso ndondomeko zothetsera umphawi zikulimbikitsa kusamala zachilengedwe pofika mchaka cha 2020
- 15.a Kusonkhanitsa ndi kuchulutsa ndalama kuchokera kumadera osiyasiyana ndi cholinga chosamalira zachilengedwe
- 15.b Kusokhanitsa ndalama kuchokera ku madera ndi magawo osiyanasiyana zoyendetsera kasamalidwe ka nkhalango ndikupereka chilimbikitso kumaiko okwera kumene kuti akhale ndi chidwi chosamalira ndi kubwezeretsa nkhalango
- 15.c Kulimbikitsa ntchito yothana ndi mchitidwe wakupha ndi kuzembetsa nyama zotetezedwa makamaka powapatsa anthu okhala mmadera aku midzi luso ndi kuthekera kokhala ndi mwayi wopeza zinthu zofunika pamoyo wawo



CHOLINGA 16



Kulimbikitsa mtendere ndi chitukuko chokhazikika kwa wina aliyense, kuwonetsetsa kuti anthu onse akupeza chilungamo ndi kukhazikitsa mabungwe oyimira wina aliyense

- 16.1 Kuchepetsa mchitidwe wa nkhanza ndi imfa pena paliponse
- 16.2 Kuthetsa mchitidwe wa nkhanza, wozunza ndi kuzembetsa ana
- 16.3 Kupititsa pa tsogolo malamulo a dziko ndi maiko akunja owonetsetsa kuti anthu onse ali ndi mwayi wofanana wozeza chilungamo
- 16.4 Kuchepetsa kupezeka kwandalama ndi mfuti zopezeka opanda chilolezo, kulimbikitsa kupeza ndi kubwezeretsa katundu wobedwa komanso kuthana ndi milandu ya upandu pofika mchaka cha 2030
- 16.5 Kuchepetsa ziphuphu ndi katangale wamtundu wina uliwonse
- 16.6 Kukhazikitsa mabungwe olimbikitsa kuchita zinthu poyera
- 16.7 Kuwonetsetsa kuti aliyense akutenga gawo popereka maganizo pazinthu zokhudza moyo wawo
- 16.8 Kulimbikitsa maiko okwera kumene kutenga gawo paulamuliro wabwino wadziko lapansi
- 16.9 Kuwonetsetsa kuti aliyense ali ndi chiphanso chaunzika kuphatikizapo kalemba wakubadwa pofika mchaka cha 2030
- 16.10 Kuwonetsetsa kuti anthu akupeza uthenga ndi kuteteza ufulu wa anthu molingana ndi malamulo a dziko ndi mgwirizano wamaiko akunja
- 16.a Kulimbikitsa mabungwe ovomerezeka makamaka mmaiko okwera kumene kudzera mu mgwirizano wamaiko onse kuti akhale ndi luso ndi kuthekera popewa nkhanza ndikuthetsa mchitidwe wa uchifwamba ndi umbanda
- 16.b Kupititsa patsogolo malamulo ndi ndondomeko zolimbikitsa kusasankhana kuti chitukuko chikhazikike



CHOLINGA 17



Kulimbikitsa njira zoyendetsera mgwirizano wa maiko onse wa chitukuko chokhazikika cha chuma (Global Partnership for Sustainable Development Finance)

- 17.1 Kulimbikitsa kusokhanitsa ndalama mdziko mwanthu kuphatikizapo thandizo lochokera ku maiko akunja kupita kumaiko okwera kumene powapatsa kuthekera kotolera msonkho ndi ndalama zina
- 17.2 Maiko olemera akwaniritse lonjezo lawo lopereka thandizo lachitukuko lokwaniritsa mulingo wa 0.7 pa 100 (0.7%) iliyonse yandalama zomwe amapereka kuthandizo lachitukuko kumaiko okwera kumene ndi 0.15 (0.15%) kufikira 0.20 (0.20%) pa 100 iliyonse zomwe zaperekedwa kumaiko osauka
- 17.3 Kusokhanitsa thandizo lachuma lowonjezera kupita kumaiko okwera kumene kuchokera kumadera osiyanasiyana
- 17.4 Kuthandiza maiko okwera kumene kupeza ngongole zodalirika kudzera mu mgwirizano wa ndondomeko ndi cholinga cholimbikitsa kubweza ngongole, kukonzanso ntchito zangongole ndi kuunikanso ngongole zomwe maiko osauka amatenga kumaiko olemera
- 17.5 Kuvomereza ndi kutsatira njira zopititsira patsogolo kukhazikitsa mabizinesi mmaiko osauka

Luso Lamakono (Technology)

- 17.6 Kulimbikitsa mgwirizano wadziko lonse pogawana nzeru zasayansi, luso lakachitidwe kazinthu kamakono, pogwiritsa ntchito njira zokhazikika zomwe zimagwiritsidwa ntchito pobweretsa maiko pamodzi monga kudzera ku msonkhano wabungwe la maiko onse
- 17.7 Kulimbikitsa kupanga, kufalitsa luso losawononga chilengedwe ndi kuligawira kumaiko okwera kumene pogwiritsa ntchito mfundo zofewa ndi zovomerezeka ndi mbali zonse zokhudzidwa
- 17.8 Kukhala ndi thumba losungira luso lamakono lochitira zinthu ndi ukadaulo wasayansi kwa maiko osauka pofika mchaka cha 2017, makamaka luso lofalitsira mauthenga podzera makina a intaneti

Kuthekera kokhala ndi luso

- 17.9 Kulimbikitsa thandizo loperekerwa luso loyenera kumaiko okwera kumene ndicholinga chofuna kuthandizira ndondomeko zamaiko okwera kumene kuti akwaniritse msanamira zachitukuko zadziko lonse

Zamalonda

- 17.10 Kulimbikitsa malonda okomera maiko onse, potsatira malamulo ochita zinthu poyera posasankhana omwe ali pansi pabungwe lazamalonda ladziko lonse (World Trade Organisation), potsatira ndondomeko zomwe maikowa anamvana ku msonkhano wachitukuko wa ku Doha (Doha Development Agenda)
- 17.11 Kuchulukitsa katundu yemwe maiko osauka amagulitsa kumaiko ena kuti nawonso akhale ndi gawo lalikulu pamsika wadziko lonse, pofika mchaka cha 2020
- 17.12 Kukwaniritsa kuchotsa msonkho wamulingo wakatundu omwe maiko osauka amapatsidwa akamagulitsa katundu kumisika yakunja mogwirizana ndi mfundo zabungwe lazamalonda la dziko lonse (World Trade Organization) powonetsetsa kuti malamulo ogulira katundu kuchokera kumaiko osauka akhale ofewa ndi olimbikitsa kupanga ntchito zamalonda poyera

Zinthu zina zofunikira

Mgwirizano wa ndondomeko

- 17.13 Kulimbikitsa kukhazikika kwa chuma mmaiko onse kudzera mu mgwirizano wa ndondomeko wamaiko
- 17.14 Kulimbikitsa ndondomeko zamaiko kuti chitukuko chikhale chokhazikika
- 17.15 Kulemekeza malamulo ndi utsogoleri wamaiko kuti uthe kukhazikitsa ndondomeko zothetsera umphawi ndi kulimbikitsa chitukuko


Ubale wamabungwe okhudzidwa

- 17.16 Kulimbikitsa mgwirizano wamaiko onse pokhazikitsa chitukuko, mothandizidwa ndi mgwirizano wa mabungwe okhudzidwa omwe amasonkhanitsa thandizo, kugawana nzeru, ukadaulo, luso ndi ndalama zothandizira kukwaniritsa nsanamira za chitukuko mmaiko onse makamaka okwera kumene
- 17.17 Kulimbikitsa ndi kupititsa patsogolo mgwirizano wamabungwe aboma, mabungwe omwe siaboma, mabungwe omenyera ufulu wa anthu pogwiritsa ntchito nzeru ndi ukadaulo omwe alinawo opezera zipangizo

Zinthu zofunikira, kauniuni ndi udindo

- 17.18 Kulimbikitsa kuthekera kwa maiko okwera kumene makamaka osauka kuti azikhala ndi mauthenga apamwamba, amunthawi yoyenera, wodalirika omwe agawidwa powunikira kapezedwe kachuma posayangána kuti uyu ndi mzibambo kapena mzimayi, zaka zakubadwa, mtundu, komwe akuchokera, ulumali ndi dera lomwe akukhala ndi zina zotero pofika mchaka cha 2020
- 17.19 Kugwiritsa ntchito zinthu zomwe zilipo kale mdziko pokhazikitsa ndondomeko zowunikira mmene chitukuko chikuyendera pothandizira kapezedwe kachuma chomwe dziko likupeza pachaka mmaiko okwera kumene ndi kuwathandizanso maikowa kuwapatsa kuthekera kotha kutolera nkhani ndi kuziunika pofika mchaka cha 2030.
- 17.19 Kugwiritsa mfundo zimene zilipo kale ndicholinga chopititsa patsogolo chitukuko chokhazikika kuti chuma cha dziko chikwere mothandizidwa ndi maiko omwe akukwera kumene pofika mchaka cha 2030





Wotanthauzira Unduna Wofalitsa Nkhani

